



Malawi: Kuyikapo mtima pazatsogolo lathu pakadali pano

Mu "Malawi: Kuyikapo mtima pazatsogolo lathu pakadali pano" tikuunika zitukuko zimene dziko la Malawi lachita komanso zipsinjo zomwe dzikoli likukumana nazobe pamene likuyesetsa kuti likhale pa mdandanda wa mayiko wotukukirapo. Powunguzawunguza mavuto womwe amadza kaamba kakukwera msanga kwa chiwerengero cha anthu m'dziko muno kapenango m'mabanja, uthenga uwu ukuwonetsa ngwirizano womwe ulipo pakati pa kukwera msanga kwa chiwerengero cha anthu, kutsata njira za kulera ndi chitukuko. Uthengawu ukutsindika kufunika kwa kuthana ndi kukwera msanga kwa chiwerengero cha anthu ndi kukwaniritsa zosowa za njira za kulera zomwe sizinakwaniritsidwe ndi cholinga chochepetsa umphawi ndi kufikira zolina za chitukuko cha dziko.




Dziko la Malawi lili chindunji ndi tsogolo lopambana chifukwa liri ndi ana ambiri amene akukula ndi moyo wathanzi, chuma chomwe dziko limapeza kuchokera ku ntchito zosiyanasiyana dziko mmomwemo (GDP) ndi chokwerelapo komanso chiwerengero cha ophunzira msukulu zathu ndi chachikulu.



Ngakhale izi zili chonchi, si anthu onse amene akupindula ndi kusintha kumeneku.

Chiwerengero chenicheni cha anthu osauka chikupitilira 5 miliyoni, chimodzimodzi ndi mchaka cha 1998.¹



Chiwerengero cha anthu chikukwera kuposa mmene chuma chingakwanitsire zosowa za anthuwo. Chaka chilichonse, chiwerengero cha dziko la Malawi chimaorjezekera ndi anthu oposa 400,000. Ngati chiwerengero cha dziko chingapitirire kukwera pa mlingo umenewu, ndiye kuti chiwerengero cha dziko lino chizakwera kanayi poyelekeza ndi mmene chiliri pakali pano pomafika chaka cha 2050.²


Anthu wochulukirapo azafuna zinthu zowayenereza pa moyo wawo. Ndondomeko ya chuma cha boma (bajeti) idzakhala pa mpanipani pofunafuna kukwaniritsa zosowa zmenezi, potero boma litha kulephera kugwira ntchito zake zina za chitukuko. Izi zizachitsa kuti chuma cha dziko chisakwele.



Kusamuka kwa anthu kuphatikizapo ndi kukula kwa chiwerengero cha anthu zikupangitsa mizinda kukhala ndi anthu ochuluka zedi. Zotsatira zake ndi zoti kumakhala kovuta kwambiri kuti mizinda ikhale ndi nyumba zokwanira zokhalamo anthuwo komanso zinthu zofunikira ku ntchito zosiyanasiyana monga madzi abwino ndi magetsi.

Pamene chiwerengero cha anthu akumudzi chikukula, malo akuchepa ndipo chonde chachepta m'nthaka. Izi zikuchitsa alimi kulima malo osayenera ulimi.³

Pamene chiwerengero cha anthu chikulirakulira, chaka ndi chaka malo sakukula konse ayi.



Maiko ambiri apita patsogolo kwambiri pa chitukuko cha chuma zaka makumi angapo zapitazi, mbali ina chifukwa cha kuyang'anira bwino kukula kwa chiwerengero cha anthu.


Pamene chiwerengero cha ana omwe mai amayenera kukhala nacho chikutsika, mayikowa anali nako kuthekera kogwiritsa ntchito chuma chawo mu ntchito za chitukuko. Lero lino chuma chonse chimene mayikowa amapeza pa munthu aliyense (GNI per person) chikuposa cha dziko la Malawi.⁴

Dziko la Malawi likuyenera kutsogozla kulabandira za kukwela kwa chiwerengero cha anthu kuti lithe kufikira pa zolina zake pa chitukuko ndi kukhala dziko lotukukirapo.



Dziko la Kenya limafanana mzochitika zake ndi ziko la Malawi, koma Kenya wachita bwino pachitukuko kuposa Malawi. Chinthusi chinodzi chimene chinapangitsa dziko la Kenya kukhala lotsogola ndi chakuti dziko la Kenya linayika mtima pa ntchito yokhudza chiwerengero cha anthu ndi njira za kulera kumayambiriro komwe.⁵

Mfundu zofunikira kwambiri zomwe dziko la Malawi likuyenera kutsata kuti lipititse patsogolo chitukuko pa chuma chake ndi kukwaniritsa zosowa zimene sizinakwaniritsidwe pa ntchito za njira za kulera komanso kuchepetsa chiwerengero cha ana omwe mai amayenera kukhala nao.



Mabanja alero m'Malawi akufuna azikhala ndi ana ocheperapo (pafupifupi atatu) kusiyana ndi mmene amafunira mabanja a makedzana (ana asanu kapena asanu ndi m'modzi).⁶

Amayi ambiri akusankha kugwiritsa ntchito njira za kulera. Masiku ano amayi 42 pa amayi 100 a chi Malawi aliwonse amene ali m'mbanja akugwiritsa nchito njira za makono za kulera.

Ndipo pamene abambo akutenga nawo mbali kwatunthu chimakhala chodziwikiratu kuti mabanjavo angathe kugwiritsa ntchito njira za kulera popanda vuto lina lirlonse.⁷



Ngakhale izi zili chomwechi, mabanja akumakhalabe ndi ana ochulukirapo koposa m'mene akufunira ndipo chiwerengero cha ana omwe mmai amayenera kuhkala nao chidakali chokwera. Mmai akuyenera kuhkala ndi ana pafupifupi ana asanu ndi m'modzi (6) obadwa kwa mayi aliyense. Chifukwa chimodzi chimene zinthu zikukhalira chonchi ndi kusafikira anthu amene akufuna njira za kulera.

Mayi m'modzi mwa amayi anayi aliwonse amanena kuti sakufuna kutumbiza posakhalitsa kapena kuti basi ana akwana, koma chonsecho sakugwiritsa ntchito njira za kulera. Amayi otete amakhala kuti sanafikilidwe ngakhale amafuna njira za kulera.



Kusapeza njira za kuleraku kumachititsa chiwerengero cha amai wokhala ndi pakati posakonzekera chikwele—pafupifupi ntheke la amai oyembekezera m'dziko la Malawi amakhala kuti anali asanakonzekere kutenga pathupi.⁸

Pakati posankonzekelapa pamachitanso kuti chiwerengero cha amai komanso ana amene akulumala ngakhalenso kufa kumene chikwere. M'Malawi muno mayi mmodzi amamwalira pa maola awiri aliwonse pa zifukwa za mavuto omwe amakumana nawo pamene ali woyembekezera ngakhalenso pobeleka.⁹

Komanso pakati posankonzekelapa mathero ake atha kukhala kuchotsa pakati mnjira zoopsyaze moyo (kuchotsa pakati pogwiritsa ntchito njira zomwe zingaopsyeze moyo).

If unmet need were met...



7,000 maternal deaths would be prevented

Imfazi zikhoza kupewedwa ngati tingakwaniritse kufikira anthu amene akufuna ndi kugwirtsa ntchito njira za kulera pofika mchaka 2020. Tikanatha kupewa;

- Imfa zokwana 7,000 zodza chifukwa cha uchembere.
- Imfa za ana wokwana 354,000.¹⁰

Kodi tikanagwirtsa chuma chochuluka bwanji kuti tipewe imfazi?



Kuchokera pakali pano mpaka chaka cha 2020 zikanatitengera pafupifupi US\$74 miliyoni kuti tikafikire wina aliyense amene akufuna njira ya kulera.


Pamene chiwerengero cha anthu pa banja chinkunka chicheperachepera, chuma chomwe tingagwirtse ntchito pokwanirtsas zosowa za anthu onse nacho chikhoza kumanka chitsika, kuphatikizapo chuma chomwe tingagwirtse ntchito popitsa patsogolo ntchito za maphunziro, katemera, madzi ndi ntchito zokhuza ukhondo wabwino, uchembere wabwino komanso zonthana ndi malungo.

Boma likhoza kupulumutsa ndalama zokwana US\$118 miliyoni—ndalama zoposa zimene boma likadagwirtsas ntchito.

Family Planning
is a
Best Buy

Njira za kulera ndi njira yokhayo yomwe ingathandize kuthetsa mavuto a zachuma a mdziko komanso mbanja pakali pano.¹¹


Kuyikapo mtima pa ntchito za njira za kulera ndi kukonza tsogolo la dziko, makamaka kwa achinyamata athu.



M'Malawi muno muli achinyamata okwana 10 miliyoni—magawo awiri a magawo atatu a chiwerengero cha anthu a mdziko lino.¹²

Ngati tingakhale ndi kugwiritsa bwino ntchito mfundo komanso ndondomeko zabwino za umoyo komanso achinyamata 10 miliyoniwa angathe kutukula tsogolo la dziko mtsogolo muno.

Kukwanirtsza zosowa za uchembere wabwino wa achinyamata athu ndiyo njira imodzi yofunikira imene yingathandize achinyamatayo kufikira pa kutukula kwavo, zomwe zingathandize kutukula dziko lathu mtsogolo muno.¹³



Pamene munthu aliyense kapena banja lirlonse lasankha mmene lizichembezero akhoza kukhala ndi chiwerengero cha ana monga mwa chifuniro chawo komanso ana womwe angathe kuwasamalira.¹⁴

Njira za kulera ndi imodzi mwa njira zikuluzikulu zomwe zingapititse patsogolo chitutuko—makamaka potukula chitutuko cha pa banja komanso kulimbikitsa kukweza chuma cha dziko.



Kodi tingachitepo chiyani? Akuluakulu opanga ndondomeko za kayendetsedwe ka ntchito zosiyanasian akuyenera kulumikizana komanso kugwirira ntchito limodzi kuti:

- Avomereze ndi kugwiritsa ntchito ndondomeko yokhazikika ya chiwerengero cha anthu m'dziko ndi kuwonetsesa kuti mfundo za chiwerengero cha anthu komanso njira za kulera zikulimbikitsidwa mu ndondomeko zosiyanasiana za ntchito za boma.
- Apereke chuma chokwanira ndi zipangizo zogwiritsa ntchito popitsa patsogolo ntchito za uchembere wabwino kuphatikizapo zipangizo zothandizira njira za kulera.
- Alimbikitse anthu kuvomereza ndi kumvetsetsa bwino za njira za kulera kudzera maunthenga wosiyanasiana komanso kukambiranana pafupipafupi.
- Ayikepo mtima potukula mwayi wa machitachita ndi ntchito zoyenera pa moyo wa achinyamata, komanso kulola achinyamata kutenga mbali pa kupanga ziganizo pa zinthu zoyenera.

(Mabuku ndi Malipoti Amene Tagwiritsa Ntchito)

- 1 Ministry of Development Planning and Cooperation, *RAPID: Population and Development in Malawi* (Lilongwe, Malawi: Population Unit, Ministry of Development Planning and Cooperation, 2010).
- 2 National Statistical Office (NSO), *Analytical Report: Volume 7, Population Projections* (Zomba, Malawi: NSO, 2010); and UNDP World Population Prospects: The 2010 Revision Population Database, accessed at <http://esa.un.org/wpp/Excel-Data/population.htm>.
- 3 Malawi Government, Ministry of Natural Resources, Energy and Environment, *Malawi State of Environment and Outlook Report: Environment for Sustainable Economic Growth 2010* (Nairobi, Kenya: UNEP, 2010).
- 4 UNDP World Population Prospects: The 2008 Revision Population Database, accessed at <http://esa.un.org/unpp/>; Demographic and Health Surveys, accessed at www.measuredhs.com/start.cfm; and The World Bank's World Development Indicators Database, accessed at <http://data.worldbank.org/indicator>.
- 5 Maura Graff, "Family Planning Is a Crucial Investment for Kenya's Health and Development" (February 2012), accessed at www.prb.org/Articles/2012/kenya-family-planning.aspx, on Feb. 14, 2012.
- 6 NSO and ICF Macro, *Malawi Demographic and Health Survey 2010* (Zomba, Malawi, and Calverton, MD: NSO and ICF Macro, 2011).
- 7 Dominick Shattuck et al., "Encouraging Contraceptive Uptake by Motivating Men to Communicate About Family Planning: The Malawi Male Motivator Project," *American Journal of Public Health* 101, no. 6 (2011): 1089-95.
- 8 NSO and ICF Macro, *Malawi Demographic and Health Survey 2010*.
- 9 NSO and ICF Macro, *Malawi Demographic and Health Survey 2010*; and NSO, *Analytical Report*.
- 10 Futures Group, Special Calculations, 2012.
- 11 The Disease Control Priorities Project, *Why Contraception Is a Best Buy: Family Planning Saves Lives and Spurs Development* (Washington, DC: The World Bank, 2007), accessed at www.dcp2.org/file/70/DCPP-Contraception.pdf, on March 7, 2011; and Scott Moreland and Sandra Talbird, *Achieving the Millennium Development Goals: The Contribution of Fulfilling the Unmet Need for Family Planning* (Washington, DC: USAID, 2006).
- 12 NSO, *Analytical Report*.
- 13 Pathfinder International, *A Smart Investment: Integrating Sexual and Reproductive Health Into Multisectoral Youth Programs* (Watertown, MA: Pathfinder International, 2011), accessed at www.pathfind.org/site/DocServer/Pathfinder_A_Smart_Investment_Integrating_Sexual_and_Re.pdf?docID=19381; and Population Reference Bureau (PRB), *Improving the Reproductive Health of Sub-Saharan Africa's Youth: A Route to Achieve the Millennium Development Goals* (Washington, DC: PRB, 2010), accessed at www.prb.org/pdf10/youthchartbook.pdf.
- 14 World Health Organization, Regional Office for Africa, and United States Agency for International Development (USAID), *Repositioning Family Planning: Guidelines for Advocacy Action* (Washington, DC: USAID, 2008); and Report of Hearings by the All Party Parliamentary Group on Population, Development and Reproductive Health, *Return of the Population Growth Factor* (UK: All Party Parliamentary Group on Population, Development and Reproductive Health, 2007).

(Komwe Tatenga Zithunzi komanso zojambulajambula zina)

Photoshare:

- © 2002 Arzum Ciloglu
- © 2007 Virginia Lamprecht
- © 2010 JHUCCP
- © 2011 Hilary Schwandt/ CCP
- © 2008 Lisa Basalla
- © 2003 Sean Hawkey

Flickr:

- ILRI
- F H Mira
- mørtn'
- Scott Gregory Photography
- Khym54
- gurg

Getty Images:

- Nigel Pavitt
- Other:
- Pond 5
- Health Education Unit, Ministry of Health, Malawi
- UNFPA Malawi
- Kate Gilles

Kuthokoza

"Malawi: Kukonza Tsogolo lathu pakadali pano" ndi chida cholengezera uthenga wochirikizika kudzera munjira zosiyanasiyana. Chidachi chidapangidwa mchaka cha 2012 ndi kagulu ka anthu wogwira ntchito zosiyanasiyana ka Malawi ENGAGE komwe kamasongozedwa Ministry of Economic Planning and Development komanso Ministry of Health, ndi chithandizo cha bungwe la Population Reference Bureau (PRB) kuzela ku ntchito za 'Informing Decisionmakers to Act (IDEA).

Kabukuka kanasindikizidwa ndi chithandizo chochokera ku mnzika za kwa Ameleka kuzera ku nthambi yoona za chitutuko pa dziko la boma la Ameleka (United States Agency for International Development (USAID)) yomwe inapeleka thandizoli ku ntchito ya IDEA yomwe nambala yake ndi AID-0AA-A-10-00009. Zonse zomwe zalembedwazi zikuyimira maganizo a bungwe la Malawi ENGAGE ndi bungwe la ntchito za Population Reference Bureau osati nthambi yoona za chitutuko pa dziko la boma la Ameleka (United States Agency for International Development (USAID)) kapena boma la United States.

© 2012 Population Reference Bureau. All rights reserved.



USAID
FROM THE AMERICAN PEOPLE



INFORMING
DECISIONMAKERS
TO ACT



INFORM
EMPOWER
ADVANCE